


AHEBRI, MUTU WACHIWIRI ³

 Mutu wa 7, wa 8, wa 9, wa 10, kuyambira pamenepo kulowamo, o, mai! Mukhale ndi pensulo yanu ndi pepala, ndi chirichonse, mokonzeka, pakuti ine ndikukhulupirira Ambuye atipatsa ife nthawi yaikulu. Tsopano ife tiri . . .

²¹⁸ Paulo akumukweza ndi kumuika, mwapamalo, Ambuye Yesu. Tsopano, ngati ife titi titsirize mu izi usikuuno, Lamlungu mmawa . . . Chomwe zambiri za izi zidzalumikizana ndi Uthenga wa Lamlungu mmawa, chifukwa ndi “kulekanitsa sabata.” Ilo ndi funso lalikulu pakati pa Achisabata lero. Ndipo ine ndikukuitanirani inu nonse kuti mudzabwere ku wa Lamlungu mmawa. Pakuti, lolondola ndi liti, Loweluka kapena Lamlungu, kwa kupembedza? Kodi Baibulo limati chiani pa izo? Ndipo kotero ndiye, kaya . . . Bukhu ili likulekanitsa lamulo ndi chisomo, ndipo Ilo likukhazikitsa chimodzi chirichonse pa malo ake. Ahebri anali kuleredwa mwa lamulo, ndipo Paulo anali kuwauza iwo chomwe chisomo chinachita, ndi lamulo.

²¹⁹ Tsopano, tiyeni tingopeza maziko aang’ono awa tsopano. Ife tiyambira mmbuyo.

²²⁰ Ndiri chiyankhulire, ine ndagulapo magalasi owerengera. Mwinamwake ine ndikhoza . . . Ngati ine ndingapezeke ndikupanga—mosefukira usikuuno, ine ndiri nawo iwo. Inu mukudziwa ine ndiri yense . . . Ine ndangotsalira zaka ziwiri kuti ndikwanitse usinkhu wa zaka fifite, ndipo ine sindikupenya monga ine ndinkachitira, zinkakhala zoyandikira kwambiri kwa ine. Pamene kupenya kwanga . . . ine ndayamba kuzindikira mawu akuzilala, ine ndimaganiza ndikuyamba khungu. Ine ndinapita kokapimidwa. Adotolo anati, “Ayi. Iwe wangodutsa makumi anai, mwananga.” Chabwino, iye anati, ngati ine ndingakhale moyo mokula kokwanira, iko kukhoza kudzabwereranso kachiwiri, kudzakhalsanso ndi kupenya mwapafupi uko kachiwiri. Iye anati, “Tsopano, iwe ukumakhoza kuwerenga Baibulo lako ngati iwe ulikankhira ilo patali ndi iwe?”

²²¹ Ine ndinati, “Inde.”

²²² Anati, “Pakapita kanthawi, nkono wako sudzakhala wautali mokwanira.”

²²³ Ndipo kotero i—ine ndikuyembekeza tsopano, mu kuphunzira uku, kuti b . . . Baibulo laling’ono la Collins ili liri nazo zolembe za kukula kwabwino mwa ilo. Ine ndikhoza kuliwerenga ilo mwabwino ndithu. Koma pamene ife tifika mu malo aakulu, okuya mmene ife titi tidzatenge Chipangano Chatsopano ndi Chakale, ndi kuzilumikiza izo palimodzi. Ine ndiri ndi la Scofield laling’ono. Ndipo ine ndinazolowera

Baibulo la Scofield, kugawaniza kwake. Ine sindimawerenga ndemanga za Scofield tsopano, chifukwa ine sindimagwirizana ndi Scofield pa zochulukana z—za malingaliro ake. Koma i—ine ndimakonda momwe analiyalira ilo, chifukwa nd. . . Ine ndakhala nalo ilo kwa nthawi yaitali, ndipo ndaliwerenga ilo, ndipo mochulukana kwambiri, mpaka ndimakhalana ngati ndimadziwa pomwe ndingapeze phunziro langa.

224 Zonse izi ndi zatsopano kwa ine, za kuphunzitsa, ndipo ine sindiri mochulukana mphunzitsi. Koma, inu mupirire nane ine kwa kanthawi pang’ono, ine ndikuuzani inu Choonadi monga momwe ine ndikudziwira Izo, mulimonse.

225 Tsopano, Bukhu ili ndi Paulo, kumbukirani. Iye anali. . . Kodi ife tinamupeza chotani iye? Iye anali mphunzitsi wamkulu, pa kuyamba pomwe, kapena sikolala wamkulu. Ndipo iye anaphunzitsidwa mwa Chipangano Chakale. Kodi winawake angakhoze kundiuza ine tsopano yemwe tinapeza kuti anali mphunzitsi wake? [Osonkhana ati, “Gamalieli.”—Mkonzi.] Gamalieli, mmodzi wa aphunzitsi odziwika a tsikulo. Ndiyeno Paulo, ife tinadzapeza kuti, tsiku lina. . .

226 Iye asanatchedwe *Paulo*, kodi winawake angandiuze ine lomwe dzina lake linali? [Osonkhana ati, “Sauli.”—Mkonzi.] Sauli. Ndipo iye anali waulamuliro wawukulu mu Yerusalemu, ulamuliro wachipembedzo. Ndipo iye anafika pamwamba ngati w—wophunzitsidwa weniweni, munthu wachipembedzo. Iye ankakhoza kuyankhula zinenero zinai kapena zisanu zosiyana, ndipo munthu wanzeru kwambiri. Chabwino, kodi maphunziro ake ndi nzeru zake zinamuthandiza iye? Ayi. Iye anati iye anayenera kuiwala zonse zomwe iye ankazidziwa, polinga kuti aphunzire Khristu.

227 Kotero ife tikupeza kuti, ndiye, izo sizimatengera munthu wanzeru kapena munthu wophunzira. Izo zimatengera—munthu yemwe ali wololera kuti adzichepetse yekha pamaso pa Mulungu, osasamala kuti mmotani.

228 Kodi inu mumadziwa kuti Dwight Moody a—analizosaphunzira kwambiri mpaka, moona, zolembe zake zinali zosauka monga ine sindikudziwa kuti chiani. Iwo ankachita kumukonzera mauthenga ake, nthawi zonse. I—iye anali wolembe mosauka chotero, wosaphunzira kwambiri.

229 Kodi inu mukudziwa kuti Petro ndi Yohane, a m’Baibulo, anali osaphunzira kwambiri mpaka iwo sankakhoza ngakhale kulemba dzina lawo lomwe, ndipo sakanalidziwa ilo liri patsogolo pawo? Mtumwi Petro, yemwe anali ndi mafungulo aku Ufumu, sakanalidziwa dzina lake litalembedwa patsogolo pake. Taganizani za izo. Baibulo linanena, kuti, “Iye anali mbuli ndi wosaphunzira.” Kotero, izo zikundipatsa ine mwayi. Amen. Inde, bwana. Izo zikupita mpaka panso pomwe, kupeza kuti Mulungu akhoza kuchita izo kwa munthu.

²³⁰ Tsopano, ndipo ife tikupeza kuti, mwamsanga pamene Paulo anali ndi chomuchitikira chachikulu. . . ine ndikufuna kuti ndikufunsemi inu. Kodi ndi chokuchitira kuti ubwere kwa Khristu? Kodi aliyense amakhala nacho chomuchitikira? [Osonkhana ati, “Inde.”—Mkonzi.] Inde, bwana. Inde, bwana. Ndi Kubadwa. Ndi chokuchitikira. Ndipo chotero ife tinali mu Koleji ya Chilutera, si kale litali. . .

²³¹ Ine ndinali nawo mwayi madzulo awa, mochedwa, ndimayenera kukhala ndiri uko thwelofu koloko, kukadya—ndi Tom Haire. Ndi angati anayamba amvapo za iye, wachi Irish, wotchuka, msirikari wa pemphero? Ndipo iye wakhala ali ndi M’bale Epp uyu, pa purogramu yake, ndipo akumawonekera mu malo ambiri kuno mu Amereka. Ndipo ine ndinali ndi nkhumaliro ndi iye lero. Ndipo ife tinali. . . Ine ndinali pafupi maora atatu nditachedwa. Inali pafupi hafu pasiti firii, kotala isanakwane foro, pamene ife timadya. Koma izo zinali bwino bwino. Ndipo ife tinali kukambirana pa zinthu izi, za momwe Yesu Khristu ali Mutu wa zinthu zonse.

²³² Tsopano, pamene Paulo anazipeza izi, iye anali ndi chomuchitikira ichi. Ndiyeno iye asanavomereze chomuchitikira ichi, izo zimayenera kuti zibwerere ku Baibulo. Ndipo ife tikupeza kuti i—kuti iye anachoka ndipo anapita ku fuko lina, ndipo kumeneko iye anakakhala mwa zaka zitatu, akufufuza Lemba, kuti awone ngati chomuchitikira chake chinali cholondola.

²³³ Tsopano, ife tikuzindikira kuti iye anali ndi chinthu chachikulu choti akumanizane nacho. Iye ankayenera kuti abwerere ndi kudzawuwuza mpingo wake, anthu onse, zinthu zomwe zimene iye anali atazizunza zinali zolondola.

²³⁴ Kodi inu munasowa kuchita chinachake chonga icho? Ndithudi, pafupifupi tonse tinatero, tinachita kubwereranso ndi kukanena, “Anthu aja omwe ife timawatcha ‘oyera odzigudubuzi,’ tafika popeza kuti, iwo anali kulondola.” Mukuona? Ndi zimenezo. Iye tinkayenera basi kuti titembenukire mmbuyo. Ndipo zinthu zomwe nthawiyina tinkadana nazo, ife tsopano tikuzikonda. Ndi kutembenuka, chinthu chachilendo.

²³⁵ A! Ine ndinapanga neno limenelo, la “oyera—odzigudubuzi.” Palibe chinthu choterocho. Palibe chinthu choterocho. Koma, iwo amawatchula anthu choncho, anthu achiyero. Koma palibe oyera odzigudubuzi. Palibe chinthu choterocho. Palibe zosungidwa za mpingo uliwonse zomwe zinalembedwapo monga choncho, utali wonse momwe ine ndingakhoze kuwonera, pa zipembedzo naini handiredi-sikisite chinachake, zosiyana. Palibe chipembedzo choterocho ngati oyera odzigudubuzi. Ndi d—dzina chabe lomwe Mdierekezi analimata pa Mpingo.

²³⁶ Koma iwo ankawatcha iwo, mu tsiku limenelo. . . Ndi angati akudziwa chomwe iwo anali kuwatcha iwo mu tsiku la Paulo? Opatuka. Inu mukudziwa chomwe *opatuka* chimatanthauza? “Openga.” Ndi anthu openga. Chotero, ine posachedwa basi ndizitchedwa “woyera-wodzigudubuza” ngati “wopatuka.” Sichoncho inu? Kotero ngati iwo—ngati iwo ankatchedwa choncho, ndi kumasangalala!

Ndipo kodi Yesu anati ife tizichita chiani pa izo? Iye anati, “Sangalalani, ndi kukhala okondwa mopitirira; pakuti mphotho yanu ndi yaikulu Kumwamba, pakuti motero anawazunza aneneri inu musanakhalepo.” Iwo anachita izo.

²³⁷ Anati, “Muzikhala okondwa mopitirira.” Chirichonse chiri *mopitirira* ndiko “kukwezedwa mmwamba patali,” kukondwa kwenikweni. Ndipo ophunzira, pamene iwo anapezeka oyenera kuti anyamule chitonzo cha Dzina la Yesu, iwo ankasangalala ndi chisangalalo chachikulu kuti akhoza kunyamula chitonzo cha Dzina Lake.

²³⁸ Ndipo lero, anthu ambiri lero, ngati iwo angapezeke akutchedwa oyera-odzigudubuza, iwo angawerame-pansi, “Mai! Mwinamwake ine ndimalakwitsa, pa kuyamba pomwe.”

Koma iwo anali okondwa nazo izo, “O, mai, kuti anyamule Dzinalo!”

²³⁹ Ndipo tsopano, mu zaka zana zachiwiri, iwo ankawatcha iwo “*amtanda pamsana*.” Ndi pamene Akhristu anakonda kunyamula mtanda pa msana pawo, kuti asonyezere kuti iwo anapachikidwa limodzi ndi Khristu. Iwo ankawatcha iwo *amtanda pamsana*. Tsopano ine ndikudziwa Akatolika amadzitcha okha chimenecho, koma uwo sunali mpingo wa Katolika. Uwo unali mpingo wa Chiprotestanti iwo usanatchedwe mpingo wa Chiprotestanti. Iwo sunatsutse kanthu kena koma tchimo. Chifukwa chomwe iwo ukutchedwa mpingo wa Chiprotestanti lero nchifukwa chakuti iwo unatsutsa—mbalume za Chikatolika. Koma ndi. . . Iwo, apabe, iwo sunali kagulu ka kachiphunzitsa kena pa nthawi imeneyo, pamene iwo unkatshedwa *amtanda pamsana*.

²⁴⁰ Ingopezani mbiriyakale ya Josephus ndi alembi ena, ndi *Two Babylons* la Hislop, ndi ena otero, ndipo inu mupeza kuti uko ndi kulondola, kuti iwo sanali mpingo ayi. Mpingo woyamba wa bungwe, umene unayamba wakhalapo, unali mpingo wa Katolika, pafupi zaka mazana atatu, pambuyo pa kudutsa k—kwa atumwi otsiriza. Pafupi zaka mazana atatu kenako, mpingo wa Katolika unapangidwa bungwe. Ndipo kuzunza kunayambikapo, ndipo ankawakamizira anthu kulowa mu mpingo wa Katolika, ndipo iwo anali ndi mpingo ndi boma, zitalumikizana.

²⁴¹ Izo zinali pambuyo pa, komwe kumatchedwa, kutembenuka kwa Konstantini, kuchoka ku chikunja kupita mu Chikatolika.

Koma, ngati aliyense anayamba wawerengapo mbiriyakale yake, iye sanatembenuke, zinthu zomwe iye ankachita. O, mai! Chinthu chokha chomwe iye anachitapo chachipembedzo chinali kuika mtanda pa tchalitchi cha Sophia Woyera. Ndi chinthu chokha chomwe iye anayamba wachitapo, anachita mwachipembedzo. Iye anali w—wotsutsa choonadi. Koma iwo amatcha uko k—kutembenuka kwake. Basi zikungofanana ndi zina zotchedwa kutembenuka lerozi.

²⁴² Tsopano, koma, ife tikupeza kuti, pamene Paulo anakhala atatembenuka ndipo atakhala ndi chomuchitikira chenicheni ichi, iye anali mwamtheradi atatembenuzidwira kwina.

Ndipo, inu mukudziwa, *kutembenuka* kumatanthauza “kutembenuzidwira kwina.” Iwe ukupita mbali *iyi*, ndipo iwe ndipo watembenuka ndi kuyamba kumapita ku mbali *iyi*. Inde, bwana. Ndi kutembenukira-kwina, kusintha komwe umayang’ana.

²⁴³ Ndipo Paulo, mwamsanga pamene iye anatembenuka, asanadziwe konse chomuchitikira chake. . . Tsopano, iye anali ndi chomuchitikira chododometsa.

Tsopano, ine ndikukhulupirira, pamene iwe umuvomereza Khristu, basi ngati Mpulumutsi wako wako, icho ndi chokuchitikira. Ine ndikukhulupirira, chisangalalo cha kudziwa kuti tchimo lako lakhululukidwa, zimangokondoweza mtima wako, mopitirira pitirira.

²⁴⁴ Koma ndiyeno pamene Mzimu Woyera wodala utsika, icho ndi chokuchitikira, Kubadwa kwatsopano kuja, komwe iwe sudzakuiwala konse. Iwe umakhala Mwana wa Mulungu. Ndipo ichi ndi chomwe chimachititsa izo.

“Inu mukudziwa bwanji izo, M’bale Branham?”

²⁴⁵ Tsopano, awa ndi maphunziro ophunzitsa. Anthu ambiri, Amethodisti, amayesera kunena kuti, “Iwo anafuula pamene iwo ankaulandira Iwo.” Chabwino, izo zonse nzabwino. Ngati inu munaulandira Iwo, ndipo munafuula, ziri bwino. Chifukwa inu munafuula, sichinali chizindikiro choti inu munaulandira Iwo, chifukwa ambiri anafuula ndipo sanaulandire Iwo.

²⁴⁶ Achipentekoste anati, “Iwo anayankhula mu malirime. Iwo anaulandira Iwo.” Izo zonse nzabwino. Ngati inu munayankhula mu malirime, ndi kuulandira Iwo, chabwino. Koma iwe ukhoza kuyankhula mu malirime ndi kusakhala nawobe Iwo. Chomwecho?

²⁴⁷ Kotero, inu mukuona, pambuyo pa zonse, ndi chokuchitikira cha kudutsa kuchokera ku imfa kupita ku Moyo; pamene zinthu zonse zakale zifa, ndi zinthu zonse nkukhala zatsopano. Khristu amakhala weniweni. Zinthu zakale zimathothoka nkuchoka, mizu yakale ya zachithupi. Inu mukudziwa momwe timakumbira muzu kuti uchokepo? Ife tinkakonda kutenga

khasu lampini ndi kungofika pansi pa iwo, ndi kuukumba iwo mpaka osakhalaponso chidutswa chotsalira mwa ilo. Ndipo iwo ankati, “Ngati pakhala pali muzu uliwonse wa chowawa ukuphuka mwa iwe, ugwire iwo utuluke.” Ndiko kulondola. Ndipo nzomwe Mzimu Woyera umachita, umazula mizu yonse. Kuikumbira panja iyo. Kuiwunjika iyo apo; kuiwotcha iyo. Kuthana nayo iyo. Inu mukhala ndi mbewu yabwino ndiye, ngati ife tichita izo.

²⁴⁸ Tsopano, Paulo ankadziwa kuti chinachake chinachitika, kotero iye anabwerera napita mu Arabia, ndipo kumeneko iye anakaphunzira kwa zaka zitatu pa aneneri onse a Chipangano Chakale, momwe iwo ankaloserera. Ndipo iye anafika popeza kuti Izo zinali mwamtheradi Choonadi.

²⁴⁹ Tsopano, fanizirani izo ndi lero, onani, pa chokuchitikira ichi chomwe ife tinali nacho kuno pa mpingo waung’ono uno: cha Nyenyezi Yammawa kuwonekera mmwamba, Kuwala kwakukulu kuja komwe kunabwera pansi, komwe kumaneneratu ndi kusonyeza zinthu zoti zichitike. Inu mukudziwa, izo nzododometsa. Koma m’bale wanga wotumikira anandiuza ine, “Uyo anali Mdierekezi.” Ndipo i—ine sindikanakhoza kumvetsa izo.

²⁵⁰ Kotero, ine sindinanene kanthu pa izo mpaka usiku wina, uko kunali chondichitikira chinachitika kutali kumtunda uko ku Chigayo cha a Green, Indiana, pamene Mngelo wa Ambuye anayenda pansipo ndipo anadzaima pamenepo, ndipo anatsimikizira izo mwa Lemba. Ndiye izo zinayatsa moto. Ndiye izo zinayamba kupita.

²⁵¹ Ndipo si patali kuposa Lamlungu lapitali, ife tinawona zisonyezo zosatsutsika za Yesu Khristu, yemwe angakhoze kumutenga munthu yemwe sanayambe wayendapo, ndi... Msempha wake womuimika palibe, pamene a Mayo ndi madotolo opambana anati, “Uwo watha, kwanthawizonse.” Ndipo atakhala wakhungu; anauka apo ndipo anayenda natuluka mnyumbayi, akukankha chikuku chake akutsika masitepe, akukhoza kuyenda ndi kupenya monga wina aliyense. Izo zikusonyeza kuti ndi mphamvu ya Ambuye Yesu wowukitsidwa. Ndi izo apo. Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.

²⁵² Kotero kodi ife si gulu lokondwa usikuuno, kudziwa kuti Mulungu watsimikizira chotichitikira chachikulu ichi chomwe ife tiri nacho, kuti chikhoza kufaniziridwa ndi Baibulo Lake limodzi ndi malonjezo? Chotero ife tiyenera kukhala tiri okondwa mopitirira. Ndipo ife tikuzindikira ndiye, kuti mu mutu wa 2, ife tapeza kuti, “Ife tisamazilole zinthu izi...Ife tisamazinyalanyaze zinthu izi.” Ife tizigwira molimba zinthu zimenezo.

Ndipo *kodi ife tidzathawa bwanji, ngati tichinyalanyaza chipulumutso chachikulu chotero; . . .*

²⁵³ Kodi ife tidzachita chiani, mu kuwala kwa Mawu a Mulungu, pamene ife tidzaima pa Malo Achiweruzo? Inu simunganene kuti, “Ine sindinali kudziwa kusiyana kulikonse.” O, inde, inu munali. “Chabwino, tsopano, M’bale Branham akhoza kukhala kuti amalakwitsa.” Izo nzoona. Koma Mulungu Sali kulakwitsa. Mawu Ake sali kulakwitsa. Ndipo tangoganizani, za chinthu chomwecho, Baibulo, lomwe nthawiyina linkakhala moyo mwa atumwi, likukhala moyo kachiwiri. O, lodala likhale Dzina la Ambuye!

²⁵⁴ Pamene ine ndikuganiza kuti ine ndiri usinkhu wa zaka foteyiti, ndikuyandikira fifite, ndipo masiku aunyamata wanga apita, ndi zina zotero; kudziwa kuti kuyambira ndiri mnyamata wamng’ono kuti ine ndakhala ndiri nalo Lonjezo lodala ili, ndipo ine ndalilengeza Ilo kwa abale anga ndi alongo; ndi kuwona kuti kwenikweni zikwi za iwo ndi omwe achoka mu mdima, kudziwa kuti ife tikupita Kwathu Kwamuyaya, kwa odala. “Ndipo ngati msasa wa padziko uno ukhala utasungunuka,” ine ndisanatsirize kulalikiraku, “pali wina ukutiyembekezera ife kutsidyako.” Aleluya! Kudziwa kuti pali madazeni a anthu akhala pano, omwe, ngati iwo angachoke mu moyo uno pakali pano; ife tisanatengere thupi lawo kwa oyika mmanda, iwo akanakhala ali mu thupi laulemerero kutsidyako, akusangalala ndi oyera a Mulungu, ali kale mu Kukhalapo kwa Mulungu, kuti azikakhala moyo kwanthawizonse. Ndi kutsimikiziridwa kwangwiro, mwamtheradi kuti ziri chomwecho! Amen!

²⁵⁵ O, izo zingawapangitse Achipresbateria kufuula! Anatero Lamlungu, sichoncho izo? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Anthu amenewo anali Achipresbateria. Ndithudi angatero, kuti aganizire. O, palibe zodabwitsa kuti anthu amafika potengeka! Pakuti, ngati iwe ufika potengeka pa kumenya mpira kapena poponyera wina mu dengu, ndi mochuluka bwanji zingakupangitse iwe kutengeka podziwa kuti iwe wadutsa kuchokera ku imfa wapita ku Moyo, kuti ndiwe Chirengedwe chatsopano mwa Khristu! Iwe ukudziwa izo mwa njira yomwe mzimu wako ukukutogolerera iwe kuchoka ku njiru, ndi kuipidwa, ndi udani, ndi zinthu zonse za mdziko. Ndipo mtima wako wakhazikika mwachirikati pa Khristu. Ndizo zolinga zako. Ndizo zonse zomwe iwe umazilingalira mu malingaliro ako, pa mtima wako, tsiku lonse ndi usiku. Pamene iwe upita kukagona usiku, ndi kuika manja ako kumbuyo kwako, monga *chonchi*, ndi kungogona pamenepo ndi kumamutamanda Iye mpaka iwe utagona. Kudzuka apo, mmawa, ukumutamandabe Iye. Amen! O, mai!

²⁵⁶ Ine ndimayesera kumutamanda Iye. Mmawa uliwonse ife takhala tikumadzuka pafupi foro koloko, M’bale Woods ndi ine, kupita uko molawirira mmawa, kupita kokasaka

agologolo. Ine ndimamutamanda Iye pansi pa mtengo uliwonse, ine ndikukhulupirira, kwa womwe ine ndingafikepo. Ine sindingakhoze kuwuwona mtengo, popanda kumutamanda Iye. Kuganiza, Iye anameretsa mtengo umenewo. Kuchiwona chiwala chaching'ono chikuwuluka; Iye akuchidziwa chiwala chimenecho. "O," inu mukuti, "zamkhutu, M'bale Bill." O, ayi, si choncho. Iye amadziwa konse komwe gologolo ali. Iye amadziwa konse komwe gulugufe ali.

²⁵⁷ Pakuti, pa nthawi ina, Iye anasowa ndalama zina, ndipo Iye anati, "Petro, uko kuli nsomba, kanthawi kapitako, inameza ndalama, yongokwanira, monga momwe ife tikuisowa. Pita ukaponye mbeza. Ine ndiitumiza iyo kumeneko. Ukachotse ndalama iyo mkamwa mwakemo, chifukwa iyo singakhoze kuigwiritsa ntchito iyo, iyomwini. Upite ukamulipire chakhumi chathu ndi chopereka." Amen.

²⁵⁸ Ndipo masabata angapo apitawo, ine ndinaiwona nsomba yaing'ono itaphedwa, itagona mmadzi. Nonse inu munaimva nkhani yake. Apo pali M'bale Woods, ndi m'bale wake ndi iwo pano oti achitire umboni izo. Nsomba yaing'ono iyo itagona yakufa kwa theka la ora, pa madzi, ili ndi makha ake atasololedwera mkamwa mwake. Ndipo Mzimu Woyera waukulu unasesera pansi, Iye atayankhula kale, dzulo lake, "Iwe uwona chiwukitsiro cha kanyama kakang'ono." Ndipo mmawa wotsatra pafupi, dzuwa litatuluka pang'ono, ife tinawona kansomba kakang'ono ako, kosati kuposa kutalika *chomwechi*. Pamene Mzimu wa Ambuye unabwera pansi, ndipo unati, "Kansomba kakang'ono, Yesu Khristu akukupanga iwe wamphumphu." Ndipo kansomba kakufa ako, kanali kakuyandama pamwamba pa madzi kwa pafupi theka la ora, kanabwerera ku moyo ndipo kanasambira kupita molimba basi momwe iko kakanathera. O, lodala likhale Dzina la Ambuye. Momwe Iye aliri wodabwitsa!

²⁵⁹ Palibe zodabwitsa Paulo akanakhoza kunena, kuti, "Iye anali mwa dongosolo la Melkizedeki." Iye anali Melkizedeki. "Melkizedeki analibe chiyambi cha masiku. Iye analibe mathero a zaka. Iye analibe chiyambi cha moyo kapena mathero a moyo. Iye analibe abambo ngakhale amayi." Koteri, Iye sakanakhoza kukhala wina aliyense. Yense yemwe Iye anali, Iye ali moyo panobe usikuuno. Choteri, Iye ali mtundu wokha wa Moyo Wamuyaya, ndipo uwo ndi wa Mulungu.

²⁶⁰ Usiku wathawu pamene ife tinali ndi zokambirana, m'bale samakhoza kumvetsa utatu wa Mulungu, ndi momwe ife tinali kuyankhulira za iwo. Momwe kuti Yesu anaima apo, Munthu, wa pafupi usinkhu wa zaka sate. Ndipo Iye anati . . .

Iwo anati, "O, makolo athu ankadya mana mu chipululu."

²⁶¹ Iye anati, "Ndipo iwo ali, aliyense, okufa." Koma Iye anati, "Ine ndine Mkate wa Moyo uwo umene unkabwera kuchokera

kwa Mulungu kuchokera Kumwamba, umene munthu akawudya ndipo samafa.”

262 “O,” iwo anati, “makolo athu ankamwa kuchokera ku Thanthwe mu chipululu.”

263 Iye anati, “Ine ndine Thanthwe Limenelo.” Mwamuna wa usinkhu wa zaka sate. Anati, “Abrahamu anasangalala pa kuliwona tsiku Langa.”

264 “Bwanji,” anati, “tsopano Iwe ukutanthauza kuti undiuze ine kuti Ndiwe wamkulu monga Abrahamu, ndipo Sindiwe wa zaka fifite panobe, ndipo ukutanthauza kunena kuti Iwe unamuwona Abrahamu yemwe wakhala atafa kwa zaka mazana asanu ndi atatu? Ife tikudziwa kuti Iwe uli ndi mdierekezi tsopano. Ndiwe wopenga.” Ndi zomwe. . . Ndi chomwe *mdierekezi* chimatanthauza, munthu “wopenga.” Anati, “Iwe uli ndi mdierekezi, ndipo Ndiwe wamisala.”

265 Iye anati, “Asanakhalepo Abrahamu, INE NDINE.”

266 Ndi yemwe Iye anali. Iye sanali munthu wamba chabe, ngakhalenso Iye sanali mneneri. Iye anali Mulungu, Mulungu akukhala padziko lapansi mu thupi la mnofu lotchedwa “Yesu,” Mwana wa Mulungu m—muthupi. Ndizo ndendende yemwe Iye anali.

267 Tsopano, ife tikumupeza Iye cha apa, kuti mu gawo lotsiriza tsopano, la kutsekera kwa mutu wa 2, komwe ine ndikufuna kuti ndifikeko, kuyambira ndi ndime ya 16, kapena ndime ya 15.

Ndipo anawawombola iwo. . . kupyolera mu mantha a imfa—a imfa anali nthawi ya moyo wawo wonse ogonjera ku ukapolo.

Ndi zomwe iye ananena kuti Yesu anachita, kuti Iye anabwera kuti adzawawombole iwo ku nsinga, omwe anakhala ali mu mantha a imfa nthawi ya moyo wawo yonse.

268 Tsopano palibe chofunikira kuwopera imfa. Tsopano, ndithudi, ife timatero; ife, palibe mmodzi wa ife amafuna kutero, chomwe ife timachitcha, *kufa*. Koma kodi inu mukudziwa kuti ngati munthu ali wobadwa kachiwiri iye sangakhoze kufa? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Iye angakhoze bwanji kukhala nawo Moyo Wamuyaya ndiyeno nkufa? Iye sangakhoze kuchita izo. Chinthu chokha chomwe chiri imfa, mawu okuti *imfa*, amatanthauza “kulekanitsidwa.” Tsopano iye angatilekanitse kuchokera pa kukhalapo kwa maso athu. Koma iye ali nthawizonse mu Kukhalapo kwa Mulungu, ndipo nthawizonse azikhala ali. Chotero, imfa si chinthu chovuta. Imfa ndi chinthu chaulemerero. Imfa ndi chomwe chimatitengera ife kupita mu Kukhalapo kwa Mulungu.

269 Koma tsopano, ndithudi, ife, pokhala a umunthu, ife timayenda mu zinthu izi za mdima kuno, i—ife sitimamvetsa izo momwe ife timayenerera. Ndipo, ndithudi, pamene

kutsamwitsa kwa imfa kudza, iyo imapangitsa woyeretsetsa kumene mwa ife kuchita mantha ndi kubwerera mmbuyo. Iyo inamupangitsa Mwana wa Mulungu kunena, “Kodi chikho ichi chingandipitirire?” Iyo ndi chinthu chowopsya. Musati mumvetse izo molakwitsa. Chifukwa ife. . . Iyo ndi chilango cha tchimo, imfa ili, ndipo iyo ikuyenera kukhala ili yowopsya.

Koma ngati ife tingakhoze kuyang’ana kungodutsa chotchinga, kutaliko, uko ndi komwe izo ziri. Adalitsidwe Ambuye! Kungodutsa chotchinga, ndi komwe munthu akukhumba kuyang’anako usikuuno. Anna Mae Snelling wamng’ono ndi iwo anakonda kuimba nyimbo kuno, “Ambuye, Ndiroleni Ine Ndiyang’ane Kudutsa Chotchinga cha Nthawi.” Aliyense akufuna kuti awone izo.

²⁷⁰ Tsopano, tsopano ife tiri apa, mu ndime ya 16. “Pakuti ndithudi Iye anatenga. . .”

Pakuti ndithudi iye sanadzitengere pa iye, pa iye chikhalidwe cha angelo; koma iye anadzitengera pa iye mbewu ya Abrahamu.

²⁷¹ O, ife tikufuna kuti tigwiritse kwa izo kachiwiri tsopano. Tsopano ife tikubwera chotsika kumene kuti tifiike. . . Chifukwa, gawo loyamba la mutu wa 3 uwu, gawo lotsiriza la iwo, likulumikizana umo pa “tsiku lija la sabata,” za Lamlungu likudza ili.

²⁷² Tsopano penyani.

. . . iye sanatenge. . . chikhalidwe cha angelo; . . .

Tsopano, kodi ndi ndani “Iye,” akumukambayo? Khristu. Khristu ndi ndani? Mulungu, Logosi ya Mulungu.

²⁷³ Tsopano ndiroleni ine ndifotokoze izi kachiwiri, chotero inu mukhale otsimikiza. Mulungu si Amulungu atatu. Utatu wa Mulungu ndi Mmodzi. Atate, Mwana, Mzimu Woyera, sizimatanthauza kuti pali Amulungu atatu osiyana. Ngati izo ziri, ife tikanakhala tiri achikunja. Ndicho chifukwa Ayuda sangakhoze kumvetsa. Sizinaphunzitsidwepo konse mu Baibulo. Tsopano, izo zimaphunzitsidwa mu mpingo wa Chikatolika, mwamtheradi, apo ndi pamene ubatizo wa utatu unachokera.

²⁷⁴ Mu Afrika iwo amakubatiza iwe katatu chafufumimba: kamodzi kwa Mulungu Atate; kamodzi kwa Mulungu Mwana; kamodzi kwa Mulungu Mzimu Woyera. Tsopano, uko ndi kulakwitsa. Mulibe kuphunzitsa kotero kwa izo mu Baibulo. Mukuona?

²⁷⁵ Ndipo tsopano, izo—ndizo zomwe iwo ankaphunzitsa. Izo zinabwera mmusimo kupyolera mwa Lutera; kuchokera kwa Lutera, kupita kwa Wesile; kupitirira mmusimo kudzalowa mu mibadwo pamene iyo inkapitirira nazo. Koma izo sizinali konse chiphunzitsa cha Baibulo. Izo nthawizonse zakhala ziri zolakwitsa, kuchokera pomwe izo zinayambira.

276 Tsopano, chotero, Mulungu anali pachiyambi. Kusanakhale kuli kuwala kulikonse, kusanakhale kuli atomu konse, kusanakhale konse kuli nyenyezi, kusanakhale konse kuli chinthu chowoneka chirichonse, Mulungu ankadzaza danga lonse. Ndipo Mmenemo munalibe kanthu koma ungwiro: chikondi changwiro, chiyero changwiro, chilungamo changwiro. Iwo unali Mzimu. Iye anadzaza danga lonse konse kuchokera ku Muyaya, komwe ife sitingakhoze kuzilingalira Izo. Izo zimapyola chirichonse chomwe ife tikanakhoza kuchilingalira.

277 Monga kupyolera pa galasi ilo, ife tikhoza kuwona—zana ndi zaka milioni zina za danga la kuwala. Taganizani za izo. Zaka milioni zana za danga la kuwala. Ndipo kuwala—kuwala kumathamanga pafupi mailosi zikwi eyiti pa mphindi. Ndipo zaka milioni zana za danga la kuwala . . . Tangoganizani ndi mailosi mamilioni angati omwe awo akanati akhale ali. Inu simukanakhoza nkomwe kuwerengera iwo. Inu mukanakhoza kungotenga mzere wa manaini ndi kuwayendetsa iwo kuzungulira nawo Jeffersonville, ndipo apobe inu simukanakhoza kuziswera izo mma mailosi a mailosi. Taganizani za izo. Ndipo kupitirira zimenezo kudakali nyenyezi ndi maiko. Ndipo Mulungu, chimodzi cha izo chisanakhalepo, Iye anali alipo. Mukuona?

278 Ndipo tsopano Logosi yomwe inapita kuchokera kwa Mulungu, yomwe inali—Logosi, zonse izi zinayamba kuwumbika kukhala—mawonekedwe a thupi. Ndipo mawonekedwe a thupi awa anali kutchedwa, mu kuphunzitsa kwa usikolala, Logosi, Logosi yomwe inapita kuchokera kwa Mulungu. Mwa kuyankhula kwina, m—mawu abwinoko a izo, anali chomwe ife timachitcha fiofane. (Fiofane ndi thupi laumunthu lomwe liri laulemerero.) Osati ndendende ndi mnofu ndi magazi ngati izo zidzakhala ziri tikadzafika mwaulemerero, koma izo ziri mwa maonekedwe a thupi laumunthu lomwe silimadya, ngakhalenso ilo silimamwa, koma n—ndi thupi, thupi lomwe likutiyeembekezera ife mwamsanga pamene ife tichoka mu ili. Tsopano, mmenemo, ife timalowa mu thupi limenelo. Ndipo uwo ndi mtundu wa thupi lomwe Mulungu anali, pakuti Iye anati, “Tiyeni ife tipange munthu mwa uthunthu wathu yomwe ndi mu mafananidwe athu.”

279 Tsopano, pamene munthu anakhala ali mu thupi limenelo, iye anali nawo ulamuliro pa nsomba zonse, ndi mbalame, ndi—zinyama za kuthengo. “Ndiyeno apo panalibe munthu woti azilima mu nthaka,” Genesis 2. Iye anali atamupanga kale wamwamuna ndi wamkazi, koma apo panalibe munthu woti azilima mu nthaka.

Ndiye Mulungu anamupanga munthu kuchokera ku fumbi la dziko lapansi. Iye anamupatsa iye dzanja l—longa la chimpanzi. Iye anamupatsa iye phazi longa la chimbalingondo. Iye anamupatsa iye, Iye anamupanga iye, pa uthunthu. Ndipo

thupi la padziko lapansi ili liri mwa uthunthu wa moyo wa chinyama, ndipo ilo linapangidwa kuchokera ku chipangizo cha mtundu womwewo. Thupi lanu linapangidwa chimodzimodzi basi ndi mtundu womwewo wa chipangizo monga kavalo, kapena galu, kapena chirichonse chonga izo. Ilo linapangidwa kuchokera ku kashiamu, potashi, mafuta, kuwala kwa dziko. Ndinu basi . . . Mnofu wonse monga uwo si mnofu wofanana; ndi mnofu wosiyana, koma ndi wopangidwa kuchokera ku fumbi la dziko lapansi komwe ilo linachokera.

Koma, kusiyana kwa pakati pa chinyama ndi munthu, Mulungu anaika solo mwa munthu, ndipo Iye sanayiike iyo mwa chinyama. Chifukwa, solo yomwe inali mwa munthu ndiyo fiofane ija.

O, i—ine, sindingafike konse ku . . . phunziro ili, koma ine ndiyenera kuti ndizitenge izi.

²⁸⁰ Taonani. Kodi inu simukukumbukira pamene Petro anali mu ndende, ndipo Mngelo wa Ambuye anabwera ndipo anadzitsegula zitseko?

²⁸¹ Iye tinali tikudutsa pa sitolo yaikulu kumtunda uko, tsiku lina, ndipo chitseko chinatseguka kutsogolo kwathu. Ine ndinati, “Inu mukudziwa, Baibulo linali nazo izo poyamba.” Mukuona? Tsopano, chitseko chodzitsegula mwa chokha.

²⁸² Ndipo pamene Petro anatuluka, kuyenda pafupi ndi alonda awa, iwo anachititsidwa khungu kwa iye. Iye anamdutsa mlonda wamkati, mlonda wakunja, kutuluka kupita pabwalo, kudutsa pa khoma, mpaka mu msewu. Ndipo palibe mmodzi wa iwo anadziwa yemwe iye anali. Ndipo sanapereke chirichonse . . . Iwo ankaganiza kuti iye anali mlonda wina kapena chinachake. Iwo . . . Iye anangodutsa apo, ndipo chitseko chinatseguka mwachokha, pamene iye anali kutuluka, ndipo chinatsekeka mmbuyo mwake. Ndipo pamene iye anatuluka kunja uko, iye ankaganiza kuti iye anali ndi loto. Ndipo iye anapita mpaka kunyumba ya Yohane Marko, komwe iwo anali ndi msonkhano wa pemphero. Ndipo iye anali kugogoda . . . [M’bale Branham akugogoda paguwa. Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi.] . . . kuti akhale ali pakati panu.

²⁸³ O, Iye ndi waulemerero. Iye ndi wodabwitsa.

Tsopano, o, *iye* sanapangidwe mwa mapangidwe a mngelo; *koma iye anadzitengera . . . mbewu ya Abrahamu*. Mulungu anakhala *mbewu ya Abrahamu*.

²⁸⁴ Tsopano, ngati ife tikanakhala nayo nthawi, kuti tipite mmbuyo ndi kukasonyeza momwe Iye ankachitira izo mu Pangano! Inu mwandimva ine ndikulalikira pa izo, nthawi zambiri, momwe iye ankatengera zinyama izo ndi kuzidula izo mzibanthu, ndi kuponyera nkhunda ndi njiwa mmenemo. Ndiye iye anayang’ana, ndipo iye anawona utsi pang’ono, wakuda woopsya, imfa. Chotsatira, ng’anjo yofuka, hade. Koma, kupyola

apo, panapita Kuwala koyera kwakung'ono. Ndipo koyera kwakung'ono uko kunapita pakati pa chibanthu chirichonse cha nsembe yodulidwa iyo, kusonyeza zomwe Iye akanati adzachite. Ndipo Iye anatenga lumbiriro, pamene Iye anachita izo, ndipo Iye analemba Pangano, kusonyeza zomwe Iye akanati adzachite.

²⁸⁵ Ndipo Iye, Yesu Khristu, anabwera ku dziko lapansi; Mulungu, *Emanuele*, “Mulungu mu thupi.” Ndipo pa Kalvare, Iye anang'ambidwa pakati. Ndipo Mzimu Wake unabwereranso pa Mpingo. Ndipo thupi Lake linanyamulidwira mmwamba ndipo linakakhala pa Mpandowachifumu wa Mulungu.

Mpandowachifumu wa Mulungu! Mmodzi yemwe ali pa Mpandowachifumuwa ndi Woweruza. Ife tikuzidziwa zimenezo. Chabwino, kodi Chiweruzocho chiri kuti? Atate apereka... Iye samaweruzwa munthu ayi. Koma Atate apereka chiweruzo chonse kwa Mwana. Chotero Iye ali... Ndipo Moyo Wake ndiwo Wansembe Wamkulu, atakhala apo ndi thupi Lake lomwe, ngati nsembe, kuti azipepesera kulapa kwathu. Amen. M'bale, izo zikuika chinachake mwa iwe.

²⁸⁶ Zindikirani, “Iye anatengapo Mbewu ya Abrahamu.” Iye anakhala Munthu. Mulungu, anapangidwa thupi pakati pathu, kuti atiwohole ife. Mwa kuyankhula kwina, Mulungu anakhala tchimo, kuti ife ochimwa tikhoze kukhala ogawana nawo ndi Iye. Ndipo pamene ife tigawana nawo za Iye, ife itimagawana nawo Zake... Ife tinali anthu a mu danga la nthawi, makumi asanu ndi awiri. Ndipo Mulungu anabwera pansu ndipo anadzakhala mmodzi wa ife, makumi asanu ndi awiri, kwa nthawi yake yoikidwa, kuti ife tikhoze kugawana nawo za Moyo Wake Wamuyaya. Ndipo pamene ife tibadwa kachiwiri, ndife ana aamuna ndi aakazi a Mulungu, ndipo tiri nawo Moyo Wamuyaya, ndipo sitidzawonongeka konse.

O, m—m—Mpulumusi wodala wake! O, palibe njira yoti tingalembe izo. Palibe njira yoti tingafotokoze izo. Izo zangokhala zopitirira kulongosola. Palibe mmodzi yemwe angakhoze kulongosola momwe Izo ziriri zazikulu. “Momwe Inu muliri wamkulu! Momwe Inu muliri wamkulu!” ndi kulondola.

Pamenepo mu zinthu zonse chinamukakamiza iye kuti apangidwe monga aliri abale Ake, . . . (Taganizani za izo.) . . . kuti iye akhoze kukhala wansembe wamkulu wachifundo ndi wokhulupirika mu zinthu zokhudza Mulungu, . . . (Mvetserani kwa izi.) . . . kuti apange chiyanjantso . . . tchimo la anthu.

Kuti ayanjanitse, tsopano, Mulungu, podziwa chilungamo, anayenera kukhala wosalungama, kuti amverere chomwe chinali kukhala uli wochimwa, kupita mmbuyo kuti ayanjanitse, kupyolera mu “chiyanjantso,” ndi kukhala nacho chifundo pa anthu.

²⁸⁷ Ndime yotsatira, mvetserani pa Izo apa.

Pakuti mwa kuti iye mwiniwake anavutika . . .

²⁸⁸ Mulungu sakanakhoza kuvutika mu Mzimu. Iye ankayenera kuti akhale mnofu, kuti amverere kuwawa kwa matenda, kuti adzamverere yesero la kusirira, kuti amverere yesero la kufuna, kuti amverere yesero la njala, kuti amverere mphamvu ya imfa. Kuti Iye akhoze kudzitengera izo pa Iyemwini kuti aime mu Kukhalapo kwa Mzimu waukulu Yehova, Mzimu, osati Munthuyo; Mzimu, kuti apange chitetezero kwa moyo uno. Ndipo Yesu anatenga zimenezo, polinga kuti apangire chitetezero kwa ife, pakuti Iye akudziwa momwe izo zimamvekera. Pamene iwe udwala, Iye amadziwa momwe inu mumamverera. Pamene inu muyesedwa, Iye amadziwa momwe inu mumamverera.

²⁸⁹ Tsopano, kodi inu munayamba mwazindikira pamene ife tikuvotera purezidenti, mlimi aliyense amavotera purezidenti yemwe anakhala ali mlimi, chifukwa iyeyo amadziwa gawo lovuta la moyo wa mlimi. Mukuona? Iye amafuna munthu wina yemwe amamvetsa.

²⁹⁰ Ndipo Mulungu asanamvetse konse; Iye pokhala Chiyero chachikulu chija. Momwe Iye akanadzakhoza kumvetsa konse, Iye atamuweruza munthu kale? Ndi chiyero Chake, Iye anamuweruza munthu. Ndipo njira yokha yomwe Iye akanati adziwire momwe angamulungamitsire munthu ndi kukhala munthu.

²⁹¹ Ndipo Mulungu anamufungatira namwali ndipo iye anabala apo thupi, osati magazi Achiyuda, osati magazi Amitundu, koma Magazi Ake Omwe. Magazi olengedwa a Mulungu, popanda kugonana umo nkomwe, iwo konse, opanda chikhumbo chakugonana. Ndipo Khungu la Magazi ili, lolengedwa mu chibelekero cha mkazi uyu, linabala Mwana. Ndipo pamene Iye ankabatizidwa ndi Yohane Mbatizi, Yohane anati, “Ine ndikuchitira umboni, kuwona Mzimu wa Mulungu (wonga nkunda) kubwera pansu ndi kukhazikika pa Iye.”

²⁹² Palibe zodabwitsa Yesu akanakhoza kunena, kuti, “Mphamvu zonse Kumwamba, ndi dziko lapansi zapatsidwa mu dzanja Langa.” Mulungu ndi munthu anakhala Mmodzi. Miyamba ndi dziko lapansi zinakumbatirana china kwa chinzake, ndipo Iye anali Mmodzi yemwe akanakhoza kupereka chiyanjantso cha tchimo lathu. Ndicho chifukwa chakuti, mu Dzina Lake, machiritso amachitika. Iye amadziwa zowawa zanu.

²⁹³ Kodi inu munayamba mwamvapo, nyimbo yakale yaing’ono iyi?

Yesu adziwa zowawa zanu, apulumutsa nachiritsa;
Tengerani katundu kwa Ambuye ndi kumusiya.

Ndiko kulondola. Iye amadziwa.

Pamene thupi livutika ululu, osapezanso
thanzi,
Kumbukirani Mulungu ayankha pemphero;
Yesu adziwa zowawa zanu, apulumutsa
nachiritsa;
Ingotengerani katundu kwa Ambuye ndi
kumusiya.

²⁹⁴ Ndizo zonse zomwe Iye akupempha, “Ingozisiyani izo pamene.” Bwanji? Iye ndi Wansembe wathu Wamkulu kuno, yemwe akudziwa momwe inu mukumverera. Ndipo Iye akudziwa momwe angakuyanjanitsireni inu kuti mubwerere ku chisomo, ndi momwe angakubwezeretsereni inu ku thanzi lanu. Iye amadziwa zonse za izo; Iye anavutika. Pamene inu mulibe malo oti mugonekepo mutu wanu; Iye anali nazo mofanana. Pamene inu muli ndi zovala za kusintha kumodzi; Iye anali nazo mofanana. Pamene inu musekedwa, kuzunzidwa; Iye anali nazo mofanana.

²⁹⁵ Mvetserani kwa ndime yotsiriza tsopano. Chabwino.

*... iye ndi wokhoza kuwathandizira iwo omwe ali
kuyesedwa.*

Kapena, mwa kuyankhula kwina, Iye ndi wokhoza *kuwateteza* iwo, *kuwathandiza* iwo, *kuwapanga* iwo... *kuchitira chifundo* nawo. Chifukwa, Mulungu Mwiniwake anakhala munthu, polinga kuti azimverere izo.

²⁹⁶ Kumbukirani, usiku wina, kodi ife sitinaphunzitse pa izo? Momwe kuti Mulungu anali nayo. . . Imfa inali ndi mbola mwa iyo, kuwopsyeza mwa iyo. “Masiku awo onse iwo anali mu nsinga za *imfa* iyi.” Ndiyeno Yesu anabwera, kuti Iye akhoze kudzachotsa mbola iyo kwa imfa.

Ndipo pamene Iye anali kukwera phiri, mukukumbukira momwe ife tinalosongolera izo? Madontho aang’ono ofiira aja pa chikhotho Chake, posakhalitsa iwo onse anadzakhala dontho limodzi lalikulu, ndi kumakhavulira Magazi pa Iye. Thupi Lake laling’ono, lofookalo, Iye sakanakhoza kupita patsogolo paliponse, ndipo Iye anagwa. Simoni waku Kurene, munthu wachikuda, anamuthandiza Iye kunyamula mtanda kukwera nawo phirilo.

Ndipo pamene iwo anamukhomera Iye pa mtanda, ndipo Iye anafuula kufuna madzi. Munthu aliyense akamaukha magazi amafuna madzi.

²⁹⁷ Mukukumbukira pamene ine ndinalalikira usiku wina za “Gwape ndi mbawala zimachita ludzu lofuna mtsinje wa madzi, chotero moyo wanga uli wefuwefu kufuna Inu, O Mulungu”? Ngati gwape wavulazidwa ndipo alimoyo, akutaya magazi, iye amayenera kuti afike ku madzi kapena iye afa.

298 Ine ndinawombeledwa, uko kumunda, pamene ine ndinali usinkhu wa zaka fortini. Ndipo ine ndinali nditagona pamenepe. Miyendo yanga itatupa pa ine, ngati chitumbuwa, kuchokera ku mfuti ya zipolopolo za muyezo wa thwelofu. Ndipo ife ndinafuula kufuna madzi, “O, ndipatseni ine okumwa!” Ine nditachita dzanzi; milomo yanga itachita dzanzi.

299 Bwanawe wanga anathamangira ku dziwe lakale, linali ndi mitundu yonse ya nyongolosi, chithaphwi. Ine sindinasamale chomwe izo zinali. Ndipo iye anadzazitsa icho ndi madzi, ndipo ine ndinatsegula kamwa yanga, ndipo iye anakanikizira chikho chake monga choncho, mkamwa mwanga. Iwe umayenera kuti upeze madzi.

300 Iye anali akutaya magazi. Iye anati, “Ndipatseni ine okumwa.” Ndipo iwo anamupatsa iye vinyo wosasa pa chinkhupule, ndipo Iye anazikana izo, ndipo sanazilole izo. Iye anali Mwanawankhosa wa Mulungu akufa mmalo mwathu, kuti abweretse chiyanjantiso kwa munthu wokhalapo. Kodi chinali chiani icho? Mulungu wa Kumwamba.

301 Billy Sunday nthawi ina, anati, “Thengo lirilonse linali ndi Angelo atakhala mmenemo, akuti, ‘Ingowongolani dzanja Lanu ndi kuloza chala Chanu, Ife tisintha zochitikazi!’”

302 Gulu lapamwamba lija la otentheka achipembedzo, lotchedwa masikolala ena aakulu ophunzira a D.D., Ph.D., anayenda pafupi ndi Iye ndipo anati, “Tsopano, ngati iwe uli Mwana wa Mulungu! Iwe unapulumutsa ena; wekha iwe sungathe kudzipulumutsa. Tsika pa mtandapo, ndipo ife tikukhulupirira iwe.”

303 Iwo sankadziwa kuti iwo anali kumuyamikira Iye. Iye akanakhoza kudzipulumutsa Yekha. Koma ngati Iye akanadzipulumutsa Yekha, ena Iye sakanati awapulumutse. Kotero, Iye anadzipereka Yekha. Lidalitsike Dzina Lake. Iye anadzipereka Yekha, kuti ine ndidzakhoze kupulumutsidwa ndipo inu mudzakhoze kupulumutsidwa. O, chikondi chosafanizitsidwa chakecho!

304 Iye sankasowa kuti adwale. Thupi lofunika lobadwa kwa namwali lija silinkasowa kuti lidwale. Koma Iye anakhala wodwala, kuti Iye akhoze kumadziwa momwe angandiimire ine pakati pamene ine ndinali kudwala.

305 Iye sankasowa kuti atope, koma Iye ankatopa. Ine ndinawerenga mbiriyakale yaing’ono nthawiyina pa izo, ine sindikudziwa ngati izo zinali zovomerezeka kapena ayi. “Pamene Iye anamuukitsa mnyamata uja waku Naini uko, kuwuka kwa akufa, Iye anakhala pa mwala nabuula ndi kupweteka kwa mutu,” chifukwa Iye ankayenera kuti anyamule matenda athu.

306 Iye ankayenera kuti anyamule tchimo lathu, ndipo apo Iye anafa, ndipo pa Kalvare pamene njuchi yakale ija ndi

imfa kamodzi inazika mbola zake. Aliyense akudziwa, pamene njuchi izika mbola yake, izo siingakhoze kuluma kenanso. Pamene njuchi iyo iwuluka nkuchokapo kapena kachilombo kalikonse komwe kamaluma, pamene iko kazika mbola yake, iyo imasololapo mbola yakeyo. Iyo imakhalabe ili njuchi koma iyo ilibe mbola. Chinthu chokha chomwe iyo ingathe kuchita ndi kulira ndi kupanga phokoso lochuluka.

³⁰⁷ Ndicho chinthu chokha chomwe imfa ingathe kuchita kwa wokhulupirira, ndi kupanga phokoso lochuluka. Koma, aleluya, lidalitsike Dzina la Ambuye, Iye anazikitsa mbola ija ya imfa mu mnofu Wake womwe. Emanuele anachita izo. Anauka kachiwiri, pa tsiku lachitatu, anazula mbolayo nkuichotsa pamenepo, ndipo ndi Wachisavundi usikuuno. Ndipo Mzimu Wake uli mu chipinda chino, ndipo Iye akudzitsimikizira Iyeyekha wamoyo pakati pathu. Ameneyo ndiye Mesiya wathu. Ameneyo ndiye Mpulumutsi wathu wodala.



BUKHU LA AHEBRI

Mauthenga khumi ndi umodzi awa a M'bale William Marrion Branham, anaperekedwa mu Chingerezi kuyambira Ogasiti 21 kudutsa Seputembala 22, 1957, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., anatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nadindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice Of God Recordings.

CHICHEWA

©2009 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org